EXAMINATION NO.: _______________

# THE MALAWI NATIONAL EXAMINATIONS BOARD

**2024 MALAWI SCHOOL CERTIFICATE OF EDUCATION EXAMINATION**

# CHICHEWA

**Subject Number: M032/III**

**Thursday, 18 July**

**Time Allowed: 2 hours**
**8:00 - 10:00 am**

## PAPER III

(Malikisi 70)

**Malangizo:**

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi awiri.**

2. Pepalali lili ndi magawo awiri: **A** ndi **B**.

3. Lembani **nambala yamayeso** pamwamba pa tsamba **lililonse la pepalali.**

4. Muchitebulo chili kumbaliku onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.

5. Perekani pepalali kwa oyangánira mayeso nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani funso ngati mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| | Total | | |

©2024 MANEB



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

CamScanner

## Gawo A (Malikisi 30)

## Nkhani za Mchezo ndi Zolembedwa

**Langizo:** Yankhani mafunso **onse** m'gawoli pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

**1. Werengani ndakatulo ili m'munsimu ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.**

### WOPHUNZIRA

Zinayi zaka zatheradi kuchitseko.
Nditutanji ine kuti anga makolo
Akamwemwetere ndi mtuka wathukuta lawo?
N'kayankhanji n'kapita wosafumbata kena?

Koma ndatolako kuno mfungulo,
Ankaimba masana ndi usiku aphunzitsi ija?
Akukokomeza kuti langa tsogolo lagona
Mwanga m'manja n'kafumbata iyo?

Kodi ndasinthanitsa wanga moyo
Ndi dansi, mpira, mowa, fodya n'zibwenzi,
Ndinkagomerazi motsutsana ndi malangizo a onse?
Apadi zinayi zathadi mwabule.

**Mafunso**

a. Ndani akuyankhula mu ndakatuloyi?

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

b. Tsimikizani kuti woyankhulayu wazindikira kuti wagwiritsa ntchito zaka zinayi mosayenera.

______________________________________________

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com
CamScanner

1. **(Continued)**

c. Fotokozani kamvekedwe ka zoyankhula mu ndakatuloyi.

______________________________

______________________________

______________________________

**(Malikisi 2)**

d. Fotokozani zomwe woyankhulayu ankachita motsutsana ndi malangizo.

______________________________

______________________________

______________________________

**(Malikisi 2)**

e. Perekani zitsanzo za zipangizo zotsatirazi zimene mlembi wagwiritsa ntchito mu ndakatuloyi.

(i) kutsinira mawu

______________________________ **(Malikisi 1)**

(ii) funso lachodziwadziwa

______________________________ **(Malikisi 1)**

(iii) kuphwanya malamulo a chiyankhulo

______________________________ **(Malikisi 1)**

f. Perekani matanthauzo a mawu awa:

(i) mtuka ______________________________ **(Malikisi 1)**

(ii) n'kafumbata ______________________________ **(Malikisi 1)**

(iii) mwabule ______________________________ **(Malikisi 1)**

g. Perekani phunziro lalikulu lomwe likupezeka mu ndakatuloyi.

______________________________ **(Malikisi 2)**

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

CamScanner

2. **Werengani nkhani ili m'munsimu mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.**

## KAMBUZI KAKAKONDWA

Tonse tidali okondwa kuti tikupita kwathu tsiku lotsatira. Uku kudali kumapeto kwa maphunziro athu pa sukulu yaukachenjede ya Takumana. Tidali titakhalapo zaka zinayi tikuchita maphunziro aukachenjede osiyanasiyana. Tsopano kuti ulendo wathu udafika kumapeto tonse tidali chimwemwe tsaya.

Monga mwachikonzero cha ophunzira tonse, atsogoleri athu azamsangulutso adaitanitsa gulu lina loimba nyimbo zamsangulutso pa usiku wotsirizawu. Gululi lidayenera kudzakanyanga nsambo kuti ife tonse tidzagwedeze matupi athu omwe pa nthawiyi adali atasasa ndi uchidakwa wamabuku.

Chipinda cha msangulutso, inde kaya kuti holo, chidakonzedwa. Matebulo onse adatulutsidwamo. Anyamata adaguliratu zakumwa zochenjera zakukhosi kwawo. Amene ankabema adapezeratu mbanje zawo. Ife asungwana tidalinso ndi gawo lathu, monga mutidziwira. Pa tsiku limeneli amayi omwe ankachita malonda okonza ndi kutsuka anthu tsitsi sadaone mpumulo. Adatanganidwa ndi kunyolola, kumanga komanso kutsuka tsitsi la asungwanafe.

Nthawi ya dansi itakwana, atsikana tonse tidali titadzipenta kumaso, mu nsidze ndi m'milomo momwe. Tidavala zovala zakumtima kwathu zogwirizana ndi zochitikazo. Anyamata adabwera atangovala movwayavwaya. Palibe yemwe adavala mochititsa chidwi munthu. Asing'anga okanyanga nsambo aja adafika. Posakhalitsa nsanja yoimbirapo idayaka moto. Padali chidansi cha fumbi kobo mu nthawi yadzinja. Sitidakhalepo ndi chisangalalo chotero m'zaka zinayi zonse za maphunziro athu. Uku kudali kutsiriza kwabwino ndipo malikhweru adali pokopoko.

Pamene usiku udanka nunyenyeka, ena amene amaliwongo adatigwira m'maso mwachangu tidapita kukadziongola pa makama athu. Ine pochoka ndidayang'ana mnzanga wogawana naye chipinda, Natasha koma sadapezeke.

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com
CamScanner

**2. (Continued)**

Mmene ndidadzidzimuka, ndidamva phokoso kunja kwa chinyumba chomwe tinkagonacho. Chapansipansi ndidamva kuti, "…. koma inu, sukulu yothaitha! Ndiye makolo ake akachilandira bwanji?"

Mosazengereza ndidaliyatsa la mtondo wadooka. Nditafika pamalopo, aliyense adali kuunika m'ngalande. Mudali chinthu m'ngalandemo. "N'chiyani kodi? Muli chiyani m'ngalandemo?''Ndidafunsa mwaphuma koma padalibe yankho lenileni lomwe ndidalandira. Kotero ndidalimba mtima kuti ndidzionere ndekha pokana kukanena zam'maluwa.

Nditangounika ndi tochi ya pa lamya yanga, chinthu chidandigunda mu mtima. Munthu adagona m'ngalandeyo adavala zovala zozionaona. Kamalaya kakuda kamilozo yoyera, kodula manja ndi kabuluku kautoto wakamtambo sizidali zovala zachilendo kwa ine. Mtima ukugunda ngati injini ya chigayo chadiziro, ndidafuna ndione kuphazi. "_ _ _ Aaa! Natashaa! Amayi Natashaa! Mayo ine! Mayo inee Natashaa!'' Adali lulaa m'ngalandemo; nsapato zothamangira zoyera zili kuphazi. Pambali pake padali chithaphwi cha magazi.

Chisangalalo chonse choti tamaliza maphunziro athu aukachenjede chidasokonezeka. Ndidali m'nkhalango yamalingaliro tsopano. Ndidayesetsa kukumbukira za usiku uja ku dansi. Kodi pali munthu wokayikitsa amene ndidamuona? Ayi, koma ndidakumbukira kuti ndidaona Natasha akutuluka panja limodzi ndi mnyamata wina dzina lake Binto. Mnyamatayu adakhala akumuvutitsa Natasha kuti ankamufuna chibwenzi koma iye ankakana. Tsono adaloleranji Natashayo kutuluka panja ndi munthu woteroyo?

Ndidatsimikizadi kuti timba adathyola mwendo dansi yothaitha. Chikondwerero chomaliza chidadula moyo wa Natasha. Dongosolo lonse litakonzedwa, gulu la ophunzira ena tidaperekeza thupi la malemu Natasha kwawo ku Mwandilanga ndipo

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com
CamScanner

2. (Continued)

zidadziwika kuti adabayidwa pamimba ndi mpeni ndi munthu yemwe sadadziwike bwinobwino pa nthawiyo.

**Mafunso**

a. Nkhaniyi ili mu mphendero yanji?

______________________________ **(Malikisi 1)**

b. Lembani malo **awiri** komwe kukuchitikira nkhaniyi.

(i) ______________________________

(ii) ______________________________ **(Malikisi 2)**

c. Perekani mfundo **ziwiri** zosonyeza kuti ophunzira a pa Takumana adatekeseka ndi chikonzero cha dansi ija.

(i) ______________________________ **(Malikisi 1)**

(ii) ______________________________ **(Malikisi 1)**

d. Tchulani dzina la mfotokozankhani mu nkhaniyi.

______________________________ **(Malikisi 1)**

e. Perekani mfundo **ziwiri** zosonyeza kuti Natasha adali wopanda masomphenya.

______________________________

______________________________ **(Malikisi 2)**

f. Fotokozani pampondachimera pa nkhaniyi.

______________________________

______________________________ **(Malikisi 2)**

g. Lembani zipangizo **zitatu** zimene mlembi wagwiritsa ntchito mu nkhaniyi.

______________________________

______________________________

______________________________ **(Malikisi 3)**

Mafunso akupitirira/...

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com
CamScanner

2. (Continued)

h. Fotokozani phunziro **limodzi** lopezeka mu nkhaniyi.

______________________________________________

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

**Gawo B** (Malikisi 40)

**Langizo:** Yankhani mafunso **awiri** okha m'gawoli m'ndime zofotokozedwa bwino.

**NTHONDO (S J Nthala)**

3. a. Fotokozani maloto **anayi** okha opezeka m'buku la Nthondo.

**(Malikisi 20)**

**KAPENA**

b. Tsimikizani popereka mfundo **zinayi** zokha kuti ampangankhani ena adali ogwirizana m'buku la Nthondo.

**(Malikisi 20)**

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com
CamScanner

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com
CamScanner

Mafunso akupitirira/...

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com
CamScanner

## CHAMDOTHE NDI ZISUDZO ZINA
(S Likongwe, W Nkhoma)

### ZIKANI

4. a. Tsimikizani popereka mfundo **zinayi** kuti kusowa umunthu ndi imodzi mwa mfundo zikuluzikulu m'chisudzochi.

(Malikisi 20)

## KAPENA

### MCHIRA WA BULUZI

b. Kuchokera m'chisudzochi, tsimikizani popereka mfundo **zinayi** kuti Nadzonzi adali waulesi.

(Malikisi 20)



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

CamScanner

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com
CamScanner

## MAFUNSO ATHERA PANO

**NB : Pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi awiri.**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com
CamScanner